EXAMINATION NO.: ______________________

CANDIDATE NAME.:______________________

# MULANJE DISTRICT COUNCIL

**THE DIRECTORATE OF EDUCATION, YOUTH AND SPORTS**

**2023 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

## CHICHEWA

## (MALIKISI 100)

**Subject Number: P032**

**Nthawi: 2 hours 15 Minutes**

**(1:00 - 3:15 pm)**

**MALANGIZO**

1. Onetsetsani kuti pepala ili liri ndi masamba **khumi (10)** osindikizidwa.
2. Onetsetsani kuti pepala ili liri ndi magawo anayi; Gawo **A, B, C** ndi **D**
3. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu pamwamba pa tsamba lililonse.
4. Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A**, ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo **B, C** ndi **D.**
6. Chongani mafunso amene mwayankha mu tebulo lili pambalipa.
7. Perekani kwa oyang'anira mayeso (invijileta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Nambala ya mafunso | Chongani funso 31-45 ngati mwayankha | Musalembe mumabokosi awa | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-11 | | | |
| 12-16 | | | |
| 17-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

**CHONDE MUSATSEGULE MASAMBA A PEPALALI MUSADAUZIDWE KUTERO.**

**©2023 MJDEYS** **Tsekulani mkati**

## GAWO A (30 MALIKISI)

**LANGIZO:**

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa Chimangirizo kapena Kalata. Mawu a Chimangirizo chanu kapena Kalata yanu asachepere 100 komanso asapyole 150.

**1.** Lembani Chimangirizo pa mutu wa: **MADZI OSEFUKIRA**

Mwa zina polemba tsatani izi:

**Ndime Yoyamba**

- Dera lomwe kudasefukila madzi
- Chaka, nthawi ndi mwezi womwe madzi adasefukira

**Ndime yachiwiri**
- Zotsatira za madzi osefukira
- Momwe anthu adathandizidwira

**Ndime yachitatu**
- Fotokozani zomwe mungachite pofuna kuthana ndi vuto losefukira madzi (2 malikisi)

**2.** Lembani kalata kwa mnzanu yomudziwitsa za masewero omwe munali nawo.

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**
- Dzina la masewero.
- Omwe mumasewera nawo.

**Ndime yachiwiri**
- Momwe masewero adathera.
- Dzina la munthu yemwe adakuyang'anirani.

**Ndime yachitatu**
- Zifukwa zomwe zipangitse kuti mupambane kapena mulephere pa masewerowo.

## GAWO B

**3. <u>Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawa</u>**

Kalekale mdziko la Kampala mudali Mfumu yotchedwa Nagoli yomwe idali yolemera kwambili. Mfumuyi idali ndi ana awiri, woyamba ankatchedwa Kanthiti ndipo wachiwiri adali Gwaza.

Mfumu Nagoli idali ndi zifuyo zochuluka monga ng'ombe, mbuzi, nkhuku, abakha ndi nkhunda. Pakhomo pake padali pa mwana alilenji. Ponena mwatchutchutchu idali mponda matiki.

Mwadzidzidzi Mfumu Nagoli inadwala koopsa ndipo idayitanitsa ana ake onse kuti ikambe nawo. Iyo idapempha ana ake aja aliyense anene zokhumba zake iyo idakali moyo.

Kanthiti adali woyamba kunena za khumbo lotenga chuma chonse cha atate ake. Wotsatira adali Gwaza yemwe adanena za khumbo lake lenileni lomwe lidali lakuti atate ake achire. Choncho Mfumu Nagoli idatenga ndodo ziwiri nipereka imodzi kwa mwana aliyense. Iyo idawalimbikitsa anawa kuti aliyense akasungitsitse ndodo yake.

Madzulo atsikulo Kanthiti adavutika mumtima. Adatenga ndodo ija naithyola ndi kuiponya pa moto. Iye adawadandaula atate ake chifukwa chomupatsa ndodo mmalo mwa chuma. M'mawa wa tsikulo Mfumu Nagoli idaitanitsa nduna zake zonse, mikoko yogona, achibale, mkazi ndi ana ake. Iyo idauza gulu lonse kuti asadzalimbane patsogolo.

Mfumuyi idauza mwana wake Kanthiti kuti atenge ndodo yake ndi kuloza chomwe akufuna. Apatu Kanthiti adangoti kakasi. Iye adayamba kulira nakalowa mnyumba mwake. Mfumu itamva zomwe Kanthiti adachita ndi ndodo yake ija, idauza Gwaza mwana wake wina kuti akatenge ndodo yake ndi kuloza zomwe akufuna. Gwaza adatenga ndodo yake ndipo adaloza chuma chonse pamodzi ndi atate ake. Pa ichi Mfumu Nagoli idauza mwana wake Gwaza kuti chuma chomwe waloza chidzakhala chake komanso poti waloza iye Mfumu, ufumunso udzakhala wake iyo ikadzamwalira. Anthu adaomba mmanja ndipo nthungululu zidamveka ponseponse.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

**a.** Kodi Mfumu Nagoli inkakhala kuti? **(1 malikisi)**

______________________________________________

**b.** Nchifukwa chiyani mfumuyo idaitanitsa ana ake? **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**c.** Tchulani zinthu ziwiri zotsimikiza kuti mfumu Nagoli idali yolemera. **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**d.** Kodi Kanthiti ndi Gwaza adalandira chiyani kuchokera kwa atate awo? **(1 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**e.** Nchifukwa chiyani Kanthiti adakhala ovutika mumtima mwake? **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**f.** Fotokozani cholinga chenicheni cha Mfumu Nagoli poitanitsa gulu la anthu pamodzi ndi banja lake. **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**g.** Perekani matanthauzo a mawu otsatirawa:

**i.** Mikoko yogona **(1 malikisi)**

______________________________________________

**ii.** Adangoti kakasi **(1 malikisi)**

______________________________________________

**h.** Nchifukwa chiyani Kanthiti adalephera kulandira chuma kuchokera kwa atate ake?

______________________________________________

______________________________________________ **(2 malikisi)**

**i.** Tchulani zinthu ziwiri zomwe Gwaza adaloza? **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**j.** Nchifukwa chiyani kudamveka nthungululu ndi mmanja pa tsiku lija? **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**k.** Perekani mutu wa nkhaniyi? **(2 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

## GAWO C (10 MALIKISI)

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa

"Koma iwe ungakagone kunyumba anzako tili khumakhuma pano", siufiti umenewu? Ndiye igwa apa mbuzi ziwiri.

**MAFUNSO**

**i.** Kodi ndi mtundu wanji wa malonje omwe mwawelengawu? **(1 maliksi)**

______________________________

**ii.** Ndani angalankhule malonjewa? **(1 malikisi)**

______________________________

**iii.** Perekani tanthauzo la nsinjiro uwu "igwa apa mbuzi ziwiri**,"** **( 1malikisi)**

______________________________

**iv.** Tchulani njira ziwiri zimene mungapewere matenda a kolera. **(2 malikisi)**

______________________________

______________________________

## KUPANGA ZIGANIZO

**5.** Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa;

**a.** gobedegobede **(1 malikisi)**

______________________________

______________________________

**b.** tsimbi **(1 malikisi)**

______________________________

______________________________

**c.** phava **(1 malikisi)**

______________________________

______________________________

**d.** gule **(1 malikisi)**

______________________________

______________________________

**e.** mperekezi **(1 malikisi)**

______________________________

______________________________

## GAWO D (4O MALIKISI)

**Zungulizani lembo lokhonza (A, B, C kapena D) mmafunso otsatirawa.**

**Mafunso 6 mpaka 11, sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mnzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**.

**6.** Analephera kuthawa chifukwa cha matope.
- **a.** Mvekero **c.** Mneni
- **b.** Mlumikizi **d.** Muwonjezi

**7.** Gulu lathu, motomoto!
- **a.** Mneni **c.** Dzina
- **b.** Mvekero **d.** Mfotokozi

**8.** Mupitebe poti atero
- **a.** Mneni **c**.Muwonjezi
- **b.** Mlumikizi **d**.Mvekero

**9.** Khasuli ndi la Zione.
- **a.** Mlumikizi **c**. Mperekezi
- **b.** Mneni **d.** Muwonjezi

**10.** Ndamukonda mtheradi
- **a.** Mlumikizi **c.** Mneni
- **b.** Muwonjezi d. Mfotokozi

**11.** Makolo athu amavala nyanda kalelo
- **a.** Mneni **c**. Mfotokozi
- **b.** Mlumikizi **d.** Mperekezi

**Mafunso 12 mpaka 16, sankhani mtundu wa afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**12.** Abambo awo ndi onyada zedi.
- **a.** Wamgwirizano **c.** Woloza
- **b.** Wakuchuluka **d.** Wa umwini

**13.** Pamsika pali mitolo yambili.
- **a.**Wakuchuluka **c**.Wowerenga
- **b.** Woloza **d.** Wamgwirizano

**14.** Khasu lomwe lasowa ndi lanu.
- **a.** Wakuchuluka **c**. Waumwini
- **b.** Wamgwirizano **d**. Woloza

**15.** Kalulu ndi nyama yochenjera.
- **a.** Wamgwirizano **c.** Wamaonekedwe
- **b.** Wogawa **d**. Wamkhalidwe

**16.** Mbuzi imodzi yabedwa.
- **a.** Ofunsa **c**. Owerenga
- **b**. Ubale **d.** Wamkhalidwe

**Mafunso 17 mpaka 20, sankhani nsinjiro za chilakhulo zomwe mayankho ake ndi omwe mwapatsidwa.**

**17.** Chinthu china chinawulultsa chomwe chinali chobisika.
- **a.** Mbuto ya kalulu idakula ntadzaonani.
- **b.** Khoswe wapadenga/ patsindwi adaululitsa wapadzala
- **c.** Mthanga kunena adapisa likongwe wa apongozi
- **d.** Wakufa sadziwika

**18.** Munthu uzisimba zokhudza iwe osati zokhudza anthu.
- **a.** Zakale zilibe ntchito
- **b.** Tikonzetikonze adanyula mtembo wa eni
- **c.** Kwa eni kulibe mkuwe
- **d.** Ulenje umasimba wako

**19.** Ukapeza mwayi wochita zinazake ndibwino kugwiritsa ntchito mwayiwo.

- **a.** Ndibwino kuti tizisunga chinsinsi chazomwe taona
- **b.** Papsa tonola sudziwa mtima wa moto
- **c.** Mako ndi mako usamuone kuchepa mwendo
- **d.** Konza kapansi kuti kammwamba katsike

**20.** Kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi kumapezetsa mavuto.

- **a.** Akuluakulu ndi mdambo mozimira moto
- **b.** Uchembere nkudyerana
- **c.** Pita uko sikuyenda
- **d.** Mapanga awiri avumbwitsa

**Mafunso 21 mpaka 25, sankhani mitundu ya alowammalo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatilazi.**

**21.** <u>Anayi</u> abwerera

- **a.** Wofunsa **c.** Woloza
- **b.** Wowerenga **d.** Wopatula

**22.** Ndi <u>wayani</u> akulirayo?

- **a.** Wowerenga **c.** Wopatula
- **b.** Wofunsa **d.** Woloza

**23.** Mwanayo wagwa <u>yekha</u>.

- **a.** Wowerenga **c.** Wotsimikiza
- **b.** Wofunsa **d.** Wodzichitira

**24.** Bukhu <u>lawo</u> labedwa.

- **a.** Umwini **c.** Wochuluka
- **b.** Woloza **d.** Wogawa

**25.** Ndigawireko <u>zowonda</u> zokha.

- **a.** Woweruza **c**. Wopatula
- **b**. Wamgwirizano **d**. Wogawa

**Mafunso 26 mpaka 30, sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**26.** <u>Zakuti adapita kusukulu</u> ndi zoona.

- **a.** Ya dzina **c.** Ya mfotokozi
- **b.** Ya muwonjezi **d.** Ya mwininkhani

**27.** Iwo adachoka <u>titatha kudya</u>.

- **a.** Ya pantherankhani
- **b.** Ya muonjezi
- **c.** Ya dzina
- **d.** Ya mfotokozi.

**28.** Abambo avala buluku <u>lomwe agula lero</u>.

- **a.** Ya dzina
- **b.** Ya mfotokozi
- **c.** Ya muwonjezi
- **d.** Ya pamthera nkhani

**29.** Yesu adafa <u>kuti tipulumuke</u>.

- **a.** Ya dzina **c.** Ya muwonjezi
- **b.** Yoima payokha **d.** Ya mfotokozi

**30.** Sizoona <u>kuti udzakhonza mayeso</u>.

- **a.** Ya muwonjezi **c**. Ya mfotokozi
- **b.** Ya dzina **d**. Yoima payokha

**Mafunso 31 mpaka 35, sankhani matanthauzo a ndagi zotsatirazi.**

**31.** Ndifera kubala.

- **a.** Mapira **c.** Chinangwa
- **b.** Nthochi **d.** Mpunga

**32.** Make mbuu, mwana mbuu.

- **a.** Chigayo **c.** Mphero
- **b.** Nankafumbwe **d.** Mtondo

**33.** Ndili ndi nkhumba zakuda.

- **a.** Mdzodzo **c.** Matayala
- **b.** Nyerere **d.** Makala

**34.** Ng'ombe yakwathu yamphuno yoyera.

**a.** Nkhwangwa **c.** Khasu
**b.** Lichero **d.** Musi
**c.**

**35.** Pansi mbandamba, kumwamba mbandamba.

**a.** Mbatata **c.** Chigwada
**b.** Chinangwa **d.** Kholowa

**Mafunso 36 mpaka 40, sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**36.** Abambo apita <u>kumunda</u>.

**a.** I-Zi **c.** U- Ma
**b.** Ku-Pa-Mu **d.** Chi- Zi

**37.** <u>Tiagalu</u> taluma nkhosa.

**a.** Mu- Mi **c.** U- Ma
**b.** Li- Ma **d.** Ka- Ti

**38.** <u>Nyumba</u> iyi yamangidwa bwino

**a.** I- Zi **c.** U- Ma
**b.** Ka- Ti **d.** Li-Ma

**39.** <u>Khasu</u> lake lathyoka.

**a.** U- Ma **c.** Li- Ma
**b.** Chi- Zi **d.** Kat-Ti

**40.** Ophunzira akuseweretsa <u>uta</u>.

**a.** a. Li-Ma **c.** Mu- Mi
**b.** U- Ma **d**. Chi- Zi

**Mafunso 41 mpaka 45, sankhani mikuluwiko yofanana matanthauzo ndi yomwe mwapatsidwa mmunsiyo**.

**41.** Apawo ndi mizu yakachere akumana pansi.

**a.** Zengerezi adalinda kwawu kwawu
**b.** Awonenji adatha mvuwu mmono
**c.** Kwa eni kulibe mkuwe
**d.** Atambwali sametana awopa kuchekana.

**42.** Kugona pakati nkuyambirira

**a.** Kutola khobwe ndi mmawa
**b.** Anthu ndi miyala sakukutika
**c.** Ndapakonda adasiya khonde
**d.** Likaomba otheratu.

**43.** Mawu akulu akoma akagonera.

**a.** Mwachaje satafuna
**b.** Maonekedwe apusitsa
**c.** Mwini phale sada chala
**d.** Mtsinje wa tinkanena unathera mu siizi

**44.** Nzeru zayekha adaviika nsima mmadzi.

**a.** Safunsa adadya phula
**b.** Ukapanda mano usamaswe phale
**c.** Wakwatira mende waleka chitute
**d.** Zathu salowa mkhola

**45.** Mutu umodzi susenza denga

**a.** Mwachaje satafuna
**b.** Nguwo yobwereka silimba mthupi
**c.** Chala chimodzi sichiswa nsabwe
**d.** Madoli adafera mchenga woyera.

**MAFUNSO ATHERA APA**

**PEPALA ILI LIRI NDI MASAMBA OKWANA KHUMI (10)**